




MUTU 1:


CHIYAMBI



A man with glasses and a beard, wearing a dark suit and tie, is seated in a large, ornate chair. He is holding an open book and appears to be reading. The setting is a library or study, with bookshelves filled with books visible in the background. The lighting is warm, suggesting a window nearby. The overall style is that of a comic book illustration.

IYI NDI NKHANI YOMWE BUKU
LAKALEKALE LIMANENA, BUKU LIMENE
LINALEMBEDWA ZAKA ZIKWIZIKWI
ZAPITAZO. MAU ALIWONSE AMENE
NDITI NDIKUUZENI NDI OONA. MAU
ENA ADZAONEKA OVUTA
KUWAKHULUPIRIRA.

KOMA
KAWIRIKAWIRI
CHOONADI CHIMAKHALA
CHACHILENDO KUSIYANA
NDI BODZA.



PACHIYAMBI, MUNTHU
WOYAMBA ASANALEDGEWE,
DZIKO LAPANSI, DZUWA,
NYENYEZI, NGAKHALE KUWALA
NDI NTHAWI ZISANALEDGEWE,
MULUNGU ANALIPO.

KOMA MULUNGU
ADAFUNA KUTI AGAWANE
NAFE MOYO WAKE.
ADAFUNA KUKHALA NDI
ABWENZI NDI ANANSI

MULUNGU ANALIPO
PACHIYAMBI, IYE MWINI ALIBE
CHIYAMBI. MULUNGU AMENEYU
ANALIPO MONGA ATATE, MWANA, NDI
MZIMU WOYERA, MULUNGU MMODZI
MWA ATATU. ATATE, MWANA, NDI
MZIMU WOYERA NDI OFANANA MU
ZONSE ZOKHUDZA UMULUNGU WAO,
NDIPO AMACHITA ZONSE PAMODZI,
POPEZA NDI MULUNGU MMODZI.
ATATE, MWANA NDI MZIMU
WOYERA AMAYANJANA
M'CHIKONDI CHOONA.



BAIBULO LIMATIENZA KUTI MULUNGU ADALENGA ANGELO
AMBIRI OSIYANASIYANA, KUTI AZIMLEMEKEZA PA
MPANDO WAKE WACHIFUMU. KOMA MMODZI MWA
ANGELOWO WOTCHEDWA LUSIFARA ADATSOGOLERA ANGELO
ENA KUTI AUKIRE MULUNGU. MULUNGU ADAWACHOTSA
ANGELOWO KUMWAMBA NDI KUWAPONYA PANZI, NDIPO
DZINA LA LUSIFARA LIDASINTHA NKUKHALA SATANA.



KOMA MUNO SITIKUKAMBA
ZA ANGELO OUKIRAWA.

MUNO TIKUKAMBA ZA
MULUNGU AMENE AMAGWIRA
NTCHITO NDI ANTHU ONSE.


ONANI TSAMBA 321 PAMENE AKULONGOSOLA MWACHIDULE
ZA BUKU LOTCHEDWA BAIBULO. KUTI MUDZIWE ZAMBIRI
ZA SATANA ONANI YESAYA 14:12-14, 45:18; EZEKIELE 28:13-
19; MATEYU 25:41; LUKA 10:18; CHIVUMBULUTSO 12:4, 20:2


PACHIYAMBI MULLUNGU
ANALENGA KUMWAMBA NDI
DZIKO LAPANSI. NDIPO DZIKO
LAPANSI LINALIBE
MAONEKEDWE ENIENI,
KOMANSO LINALI LOSAKOZEKA.
WOLENGAYO ANKAYENDAYENDA
PAMWAMBA PA MADZI.




KENAKA MULUNGU ANANENA
MAU MU MDIMA

"KUYERE"





SIMONGA MMENE ANTHU ENA LERO LINO AMAGANIZIRA. ENA AMATI PACHIYAMBI ZINTHU SIZINKAONEKA MONGA ZILILIMU. AKUTI ZINTHU ZINKASINTHA PANG'ONOPANG'ONO KUFIKIRA MMENE ZIMAONEKERAMU. KOMATU MULLINGU ADALENGA ZINTHU ZONSE PAKUNENA MAU CHABE.



NDIPO ZONSE
ZILI MONGA
MMENE
ZINALENGEDWERA
PACHIYAMBI.
PA MASIKU 6,
A MAORA 24,
MULLINGU
ADALENGA
ZOMERA NDI
NYAMA KUTI
ZIDZAZE DZIKO
LAPANSI.

MWINA 4004 B.C. - GENESIS 1:2-3




PA TSIKU LACHISANU NCHIMODZI,
WOIPAYO AKUONA, MULLINGU
ADALIMBA CHOLENGEDWA
CHAT SOPANO KUCHOKERA KUDOTHI.



MULLINGU ADAUZIRA MOYO WAKE M'THUPI
LA CHOLUMBACHO, NDIPO MUNTHU NDI
MOYO. MUNTHUYO ADALENGEDWA
M'CHIFANIZO CHA MULLINGU, NDIPO
ANAKHALA WOPOSA NYAMA ZINA ZONSE.

MULUNGU ADACHITCHULA
KUTI MUNTHU CHOLENGEDWA
CHATSOPANO CHIJA NDIPO
MUNTHUYO ADAMPATSA
DZINA LOTI ADAMU.




GENESIS 1:31, 2:7




MULUNGU ADAONA ZONSE
ZIMENE ADAZILENGA
NDIPO ANATI, ZILI
BWINO KWAMBIRI.

TSIKU NDI TSIKU
MULUNGU ANKAYANKHULA
NDI ADAMU, NDIPO MOYO
UNALI BWINO ZEDI.
MULUNGU ADABWERETSA
NYAMA ZINA ZONSE KWA
ADAMU KUTI AZITCHULE
MAINA. PAMENE
NYAMAZO ZINKADUTSA
ADAMU ADAZINDIKIRA
KUTI ANALIBE MNZAKE
PAMENE NYAMAZO
ZINALI NDI ZINZAO.



**NDIPO MULUNGU
ANATI**

**NDIDZAPAN
GA WOTI
AZIMTHANDI
ZA ADAMU.**



**MULUNGU ADAGONETSA ADAMU TULO
TOFA NATO NDIPO ADATENGA KO NTHITI
KWA IYE. NDI NTHITIYO MULUNGU
ADAPANGA MKAZI WOKONGOLA KUTI
AKHALE WOTHANDIZA ADAMUYO.**



IYEYU
NDI FUPA
LA MAFUPA ANGA,
NDI MNOFU WA
MNOFU WANGA.

MULINGU ADAMUDZUTSA ADAMU NDIPO
ADABWERETSA MKAZIYO KWA IYE. ADAWALIZA
KUTI ABEREKE ANA NADZAZE DZIKO LAPANSI.
NDIPO ADAMU ADAMUTCHA DZINA LOTI,
"HAVA," MKAZI WAKE WOKONGOLAYO.

SATANA,
WOIPAYO,
ANKANG'
OYANGANA.

ONSE AWIRI ANALI
AMALISECHE, KOMA, MONGA
MMENE AKHALIRA ANA,
SANKAZINDIKIRA ZIMENEZI.

**MUZIDYA ZIPATSO ZA
MTENGO ULIWONSE WA
M'MUNDAWU, KOMA MUSADYE
ZIPATSO ZA MU MTENGO UWU
WA PAKATI PA MUNDA, PAKUTI
PAMENE MUDZADYA ZIPATSO
ZAKEZO MUDZAFU.**

**IWO ANALI OKONDWA
MMUNDA MUJA. KUNALIBE
UCHIMO KAPENA NJALA;
SIKUNKATENTHA KWAMBIRI
KAPENA KUZIZIRA KWAMBIRI.**



**MULUNGU
ADAYANKHULAPO ZA
MITENGO, NATI...**



CHONCHO MULLINGU ADALENGA MUNDA WOKONGOLA WA PARADIZO
NDIPO ANAPATSA MPHAMVU ADAMU KUTI AZILAMULIRA ZONSE
ZA M'MUNDAWO NDI ZINTHU ZONSE ZA PA DZIKO LAPANSI.
M'MUNDAMO MUDALI ZOMERA ZAMITUNDUMITUNDU ZA MASAMBA
OKONGOLA NDI MITENGO YOSIYANASIYANA YA ZIPATSO
ZODYEDWA. KOMABE, PAKATI PA MUNDAWO PANALI MITENGO INA
IWIRI. WINA UNKATCHEDWA MTENGO WA MOYO.




MULLINGU ADALOLA ADAMU KUTI AZIDYA ZIPATSO ZA MTENGOWO PAMENE WAFUNIRA, NDIPO KUTI AKAMADYA ZIPATSO ZA MTENGOWO SANGAKALAMBE KAPENA KUDWALA KAPENANSO KUFA. MTENGO WINAWO LINKATCHEDWA MTENGO WODZIWITSA ZABWINO NDI ZOIPA. MULLINGU ADAUZA ADAMU KUTI ASAMADYE ZIPATSO ZA MU MTENGOWO.



KODI MULLINGU
WAKULUZANI KUTI
MUSAMADYE ZIPATSO ZA
M'MITENGO YONSE YA
M'MUNDAMU?


HA! SIMUDZAFU.
MUDZAKHALA OFANANA NDI
MILLINGU MUKADYA ZIPATSO ZA
MTENGOWU. MASO ANU
ADZATSEKUKA MONGA MMENE IFE
TILILI NDIPO MUDZADZIWA ZONSE
ZABWINO NDI ZOIPA.





ADATI
TIKHOZA KUDYA
ZIPATSO ZONSE ZA
M'MITENGOYI KUPATULA
UWU, TIKANGOUKHUDZA,
TIDZAFU.

SATANA ANKADANA NDI MULLINGU NDIPO ANKAFUNA
KUONONGA ZONSE ZIMENE MULLINGUYO ANKACHITA, KOMA
ANAFUNA NJIRA YOYANKHULIRANA NDI HAVA, CHONCHO
ANALOWA M'THUPI LA CHOLENGEDWA CHOKONGOLA
NAYANKHULA NDI PAKAMWA PA CHOLENGEDWACHO.



NCHOKONGOLA
LKAMACHIONA, NDIPO
CHIKUONEKA KUTI CHIKHOZADI
KUKHALA CHAKUDYA CHABWINO.
NDIPO NDIKACHIDYA
NDIDZAKHALA WANZERU, KOMA
MULLUNGU ADATI TISADYE
CHIPATSOCHI

HAVA SANKADZIWA
TANTHAUZO LA ZABWINO
NDI ZOIPA.

A woman with long, dark, wavy hair is shown from the chest up. She is looking upwards and to the right with a surprised expression. Her right hand is raised to her cheek, and her left hand is holding a round, golden fruit. The background is a bright yellow sun with rays, partially obscured by dark green leaves and branches. Another golden fruit is visible in the upper right corner.

HAVA SANAMVERE MULLUNGU
NDIPO ANADYA CHIPATSOCHO.

MOCHEDWA ANAZINDIKIRA KUTI
WANYENGEDWA. CHIPATSOCHO
CHINAMDZIWITSADI ZABWINO
NDI ZOIPA, KOMA ZOIPAZO
ZIDAYAMBA KULAMULA.

HAVA ADATENGERAKO
MWAMUNA WAKE
CHIPATSOCHO NAMUZA
KUTI NAYENSO ADYEKO.



ONA, SINDINAFE.
IDYA NDIPO UDZAKHALA
WANZERU.

GENESIS 3:1-6; CHIVUMBULUTSO 20:2

MASO AO
ANATSEGUKA NDIPO
ANKACHITA MANYAZI
CHIFUKWA CHAKUTI
ANALI AMALISECHE.

HA! HA! HA!
AKUPHANI TSOPANO!
TAONANI ZIMENE
ANANDICHITIRA.

TACHITANJI?

SITINAMVERE
MULUNGU. AKUBWERA
POSACHEDWAPA.
TIYENERA KUTI
TIBISE UMALISECHE
WATHUWU.





**ADAMU,
ULI KUTI?**

**NDINAMVA
MAU ANU KOMA
NDINKAOPA
CHIFUKWA
NDINALI
MALISECHE.**

**ANAKUUZA
NDANI KUTI NDIWE
WAMALISECHE? KODI
SIMUNANDIMVERE, NDIPO
MWADYA CHIPATSO
CHOLETSEDWACHO?**



MKAZI AMENE
MUNANDIPATSA NDIYE
WANDICHIMWITSA

GENESIS 3:6-12

MULINGU ANAFUNSA
HAVA ZIMENE
ZIDAACHITIKAZO NDIPO
HAVA ADAYANKHA KUTI:

SIIII...

NJOKA NDIYO
IDANDINYENGA. IDANDIUZA
KUTI SINDIDZAFU, KUTI NDIDZAKHALA
WOFANANA NANU, KOMA SINDINE
WOFANANA NANU. NDIKUDZIMVERA
CHISONI.



CHONCHO MULLINGU
ADATEMBERERA
NJOKA NATI KWA IYO


POPEZA
WACHITA
ZIMENEZI,
UZIDZAYENDA
NDI MIMBA YAKO
NDIPO FUMBI
LIDZAKHALA
CHAKUDYA
CHAKO.

NDIPO NDIDZAIKA
UDANI PAKATI PA MBEU
ZAKO NDI MWANA WA
MKAZIYU. MBEU ZAKO
ZIDZALUMA CHIDENDENE
CHA MWANA WA
MKAZIYU, KOMA IYE
ADZAPHWANYA MUTU
WAKO.





PANO MULLINGU AKUKAMBA ZA NKHONDO
YAM'TSOGOLO. NTHAWI IDZAFIKA PAMENE MBEU YA
MKAZI IDZAGONJETA SATANA. MUNTHU AMENEYO
ADZAOMBOLA ANTHU NDI KUWAYANJANITSANSO
NDI MULLINGU NDIPO ADZAWAPULLUMUTSA KU
TEMBERERO LA TCHIMO NDI IMFA.



GENESIS 3:13-15

MULUNGU AKADATHA KUONONGA LUSIFARA
NDI ANGELO AKE MKAMPHINDI KOCHÉPA.
KOMA ADAWALEKA NDI MOYO KUTI AZIYESA
ANTHU. KODI ANTHU ADZAMVERA MULUNGU,
KAPENA ADZATSATA SATANA WOGALUKIRAYÓ?

MULUNGU ANANENA
MAU OLANGA ANTHU

ADAMU, POPEZA UNAMVERA
MKAZI WAKO NDI KUGALLUKIRA INE,
NDIDZATEMBERERA DZIKO LAPANSI, NDIPO
NDIDZAMERETSA BWINO MINGA NDI NTHULA
KUPOSA NDIWO ZAMASAMBA, NDIPO IWE
LDZAYENERA KUGWIRA NTCHITO MOLIMBIKA
KUTI LPEZE CHAKUDYA M'NTHA-
KAMU. NTHAWI ZONSE PAMENE
LDZAKHALA NDI MOYO LDZAMVA
CHISONI, LDZAGWIRA NTCHITO NDI
THUKUTA LA PA NKHOPE YAKO
MPAKA PAMENE LDZAFANA NDI
KUBWERERA KUFUMBI KUMENE
LDACHOKERA.



TSOPANO INALI NTHAWI YOTI
ADAMU NDI HAVA AFE MONGA
MMENE MULUNGU ADAANENERA.
KOMA MMALO MOWAPHA, MULUNGU
ADAAPHA NYAMA MMALO MWAO
NATENGA ZIKOPA ZANYAMAZO KUTI
AKONZERE ZOVALA ADAMU NDI HAVA.






SADATIPHE! TILI
NDI MOYOBE!

ANAPHA NYAMA
MMALO MWA
IFE!


ADAMU NDI HAVA SANAFE
TSIKU LIMENE ADACHIMWALO,
CHIFUKWA NYAMA ZOSALAKWA
NDIZO ZIDAFU MMALO MWAO.
KOMA ZOTI ADZAFU MULLUNGU
SANABWEZE, NDIPO PAMBUYO
PAKE ADAYAMBA KUFA NDITHU.
UCHIMO UMADZETSA IMFA.

ADAMU NDI HAVA ATACHIMWA, MULLINGU
ADAWATULUTSA MMUNDA WOKONGOLA
UJA KUTI ASADYE ZA MTENGO WA MOYO
KUOPA KUTI ANGAKHALE NDI MOYO
WAMUYAYA MU UCHIMO WAOWO.

MULLINGU ADAIKA MNGELO WINA
WOTCHEDWA KERUBI PAKHOMO PA
MUNDAWO KUTI WINA ALIYENSE
ASALOWE NDI KUKAFIKA KU MTENGO
WA MOYO. PAMBUYO PAKE
MUNDAWO UDAWONONGEDWA
NDIPO MTENGO WOPATSA MOYOWO
UDACHOTSEDWA PA DZIKO LAPANSI.
TSIKU LINA Udzabweretsedwanso
ku dziko lapansi, koma tiyeni
tipitirire ndi nkhaniyi.



GENESIS 3:17-24; EZEKIELE 18:4




ADAMU NDI HAVA ADAALI NDI ANA
AMBIRI. PAMBUYO PAKE ANA AO AAMUNA
NDI AAKAZI ADAYAMBA KUKWATIRANA
NKUMAKHALA NDI ANA AOAO.




MWANA WAO WOYAMBA, KAINI, ANKALIMA
NDIWO ZAMASAMBA NDI ZIPATSO. MWANA
WAO WACHIWIRI, ABELE, ANKAWETA
ZIWETO. KODI MMODZI MWA IWO
ADZAKHALA MWANA WOLONJEZEDWA
AMENE ADZAWONONGE SATANA?

KAINI NDI ABELE ANKADZIWA
ZA MULUNGU NDI ZIMENE
ZINACHITIKIRA MAKOLO AO
MMUNDA UJA. KOMA
MULUNGU ADAALEKA KUYENDA
KAPENA KUYANKHULA NDI
ANTHU. ADAMU PAMODZI NDI
ANA AKE ADALEKANITSIDWA
NDI MULUNGU CHIFUKWA CHA
KUSAMVERA KWA ADAMUYO.
NDIPO POPANDA MULUNGU
MOYO WAO UNALI WOWAWA.



TSIKU LINA ANA AAMUNA AWIRI AJA
ADAGANIZA ZOTI APEMBEDZE MULUNGU.
ATATE AO ADAWAUZA ZAKUTI MULUNGU
ADAPHA NYAMA MMUNDA, CHONCHO MWA
CHIKHULUPIRIRO ABELE ADAPHA NYAMA
NAIPEREKA KWA MULUNGU NGATI NSEMBE.

MULUNGU,
INE NDINE
MUNTHU WOCHIMWA,
NDIKUPHA NYAMA IYI
NDI KUIPEREKA KWA
INU MMALO MWA
IMFA YANGA.



MULLUNGU,
LANDIRANI MPHATSO
IYI YA ZABWINO
ZIMENE NDINAYENERA
KUPEREKA KWA INU.

KAINI ADAPEREKA
NGATI NSEMBE
ZABWINO
ZIMENE ANALI
NAZO, KOMA
SINALI NSEMBE
YAMAGAZI. KAINI
SANADZIWE
KUTI MULLUNGU
ADAKHUMUDWA
CHIFUKWA CHA
TCHIMO LAKE.


KODI WINA MWA ANTHUWA
ADZAKHALA MPULUMUTSI
WOLONJEZEDWA?

AI, KAINI




MULUNGU ANAKANA NSEMBE YA
KAINI CHIFUKWA INALIBE MAGAZI.

MULINGU ADAKONDWERA NDI
ABELE CHIFUKWA CHA NSEMBE
YAKE. PAMENE MULINGU ADAONA
MAGAZI A NKHOSA YOSALAKWA,
ADAKHULULUKIRA ABELE.




MULINGU ADATI KWA KAINI,
"UKACHITA ZABWINO,
NDIDZAKONDWERA NAWE.
KOMANSO UZALAMULIRA
MBALE WAKO ABELE NDIPO
ADZAKHALA PANSI PA
ULAMULIRO WAKOWO."



MBALE
WANGA, NTHAWI
IKADALIPO NDIPO
UKHOZA KUPEREKA
NSEMBE
YAMAGAZI.


KODI UKUGANIZA KUTI NDIWE
WOPAMBANA? ZIPATSO ZANGA NDI
NDIWO ZAMASAMBA ZINALI ZOPOSA
NKHOSA YAMAGAZIYO. KODI
CHIKUKUCHITITSA KUKHALA
WOPAMBANA NCHIYANI? KODI IWE
NDIWE WABWINO KUPOSA INE?



USANDITAYITSE
NTHAWI!
SINDIDZAKUMVERA
NSO!

ABELE ANAPHEDWA, NDIPO
KAINI ANKAYESA KUBISA
TCHIMO LAKE LAKUPHALO.

GENESIS 4:5-8



KOMA KAINI
ANALEPHERA KUBISIRA
MULUNGU CHOIPA CHAKE.
MULUNGU AMAONA
ZONSE NDIPO
AMADZIWANSO ZONSE.

**KAINI, KODI
ALI KUTI
ABELE MBALE
WAKO?**

**MAGAZI A
MBALE WAKO
AKADALI M'NTHAKA.
AKUNDIYANKHULA ZA
CHOIPA CHAKO.**

NDINGADZIWE
BWANJI KUMENE
IYEYO ALI? KODI INE
NDINE WOYENERA
KUMAMUSAMALIRA?
SINDIKUDZIWA. SINDINE
MLONDA WA MBALE
WANGA.

MULLINGU AMADZIWA ZONSE. AMAONA ALIYENSE NTHAWI ZONSE. PALIBE CHIMENE CHINGABISIKE KWA IYE. ANAONA ZIMENE KAINI ADACHITIRA ABELE. MULLINGU ADATEMBERERA KAINI NDIPO ADATHAWIRA M'CHIPULLULU, PAMODZI NDI MKAZI WAKE. KUCHIMWA KWAKE KUDAMDZETSERA

KAINI SAKANAKHALA MPULLUMUTSI WOLONJEZEDWA. IYE MWINI ANKASOWA CHIPULLUMUTSO.

PAMENE MUNTHU WOYAMBA ADALENGEDWA ZOOPSA ZOMWE ZIMABWERA M'MATUPI A ANTHU CHIFUKWA CHOKWATIRANA PACHIBALE KUNALIBEKO, KOMA PAMBUYO PAKE ZOOPSAZO ZINAYAMBA, MULLINGU ANALAMULA KUTI ANTHU APACHIBALE ASAMAKWATIRANE.



NANGA ZA LONJEZO LA MULINGU LOTI MWANA
WAMWAMUNA ADZAKHALA MPULUMUTSI?
ADAMU NDI HAVA ANALI NDI MWANA WINA
WAMWAMUNA NDIPO ADAMUTCHA KUTI SETI.
ANABALANSO ANA ENA AAMUNA NDI AAKAZI.



MULINGU
WANDIPATSA
MWANA WINA
WAMWAMUNA KUTI
ALOWE M'MALO MWA
UJA AMENE KAINI
ANAMUPHA.

GENESIS 4:9-16, 5:4; MACHITIDWE 17:24-26



SETI ANALI NDI MWANA WAMWAMUNA, NDIPO MWANA WAKEYO
ANALINSO NDI MWANA WAMWAMUNA, NDIPO ANA AAMUNA AMBIRI
ANABADWA, KOMA PALIBE MMODZI MWA IWOWA AMENE
ANACHOTSA TEMBERERO LA TCHIMO NDI KUPHWANYA IMFA.
POSAKHALITSA DZIKO LINADZALA NDI MIZINDA, MIDZI NDI MINDA.

PA MBADWO
ULIWONSE, PAMENE
ANTHU ANKACHULUKA,
MACHIMONSO
ANKACHULUKA. ANTHU
ANKACHITA MACHIMO
A CHIWEREWERE NDIPO
ANALI ANKHANZA.
MAGANIZO AO ONSE
ANALI OCHIMWA.
PALIBE AMENE
ANKACHITA
CHILUNGAMO. ADAMU
ADACHITA TCHIMO
LIMODZI; KOMA
TSOPANO ANTHU
ANKACHITA MACHIMO
AMBIRIMBIRI.



**MULUNGU ANATI,
"NDAKHUMUDWA CHIFUKWA
CHOTI NDIDALENGA MUNTHU PA
DZIKO LAPANSI. NDIDZAONONGA
ZAMOYO ZONSE PA DZIKO
LAPANSI." SATANA, MDANI WA
UFUMU WA MULUNGU,
AKADASANGALALA KWAMBIRI
POONA KUTI MULUNGU WAPHA
ANTHU ONSE.**




MIBADWO 9 INAPITAPO (ZAKA
1,400) NDIPO DZIKO LAPANSI
LINADZALA NDI UCHIMO.

ANTHU ANKAGWIRA
UKAPOLO ANZAO.


KODI MULUNGU ADZALIPEZA
KUTI BANJA LOMUKONDA
NDI KUMUMVERA?

GENESIS 6:5-7; AROMA 5:12

PAFUPIFUPI 2500 B.C.



KOMA PANALI MUNTHU MMODZI
AMENE ANKACHITA CHILUNGAMO;
MUNTHU WA MAKHALIDWE ABWINO.
NGAKHALE KUTI MULLINGU ADAGANIZA
ZONONGA ANTHU ONSE,
ADAGANIZA ZOMCHITIRA CHIFUNDO
MUNTHU AMENEYU, OSAMUPHA IYE
PAMODZI NDI BANJA LAKE.



**NOWA, INE NDITUMIZA CHIGUMULA
CHACHIKULU CHA MADZI PA DZIKO LONSE
LAPANSI. CHOPUMA CHILICHONSE CHIDZAFI.
KUTI UDZAPULUMUKE IWE, PAMODZI NDI
BANJA LAKO NDI NYAMA, UPANGE BWATO.**


**M'BWATOMO UDZATENGEREMO NYAMA
ZIWIRIZIWIRI (YAIMUNA NDI YAIKAZI) MWA
NYAMA ZONSE ZA PA DZIKO LAPANSI.
ZONSE PAMODZI, UDZATENGE MAGULU 7 A
NYAMA ZODYEDWA. NDIDZAKULUZA MMENE
UDZAPANGIRE BWATOLO NDI MMENENSO
UDZAKONZEKERE CHIGUMULACHO.**

KODI NOWA NDIYE ADZAKHALE
MWANA WOLONJEZEDWA LIJA, AMENE
ADZAONONGE NTCHITO ZA SATANA?
KODI ADZAAMVERA MULUNGU,
KAPENA NAYENSO ADZALEPHERA?



MULUNGU ADAMUZA NOWA
MAKULIDWE A BWATO LIJA KUTI
MUDZALOWE NYAMA ZONSE
ZIMENE ADAMUZA KUTI
ADZALOWETSEMO KUPHATIKIZAPO
CHAKUDYA CHIMENE ZIZIDZADYA.

GENESIS 6:8-9, 17-22, 7:2



NOWA SADAKONDWE ATAMVA ZOTI
ANTHU ONSE ADZAONONGEKA
CHIFUKWA CHA CHIGUMULA,
NDIPO ADAYESETSA KUCHENJEZA
ANTHUWO KUTI ALEKE KUCHIMWA.

NDIKUKUCHENJEZANI KOMALIZA.
MULLINGU ADZAONONGA DZIKO LONSE
LAPANSI NDI CHIGUMULA CHACHIKULU.
MUYENERA KUNDIKHULLUPIRIRA KUTI
TIKALOWERE LIMODZI M'BWATOMO.



MULUNGU
WACHIKONDI
ANGAONONGE
BWANJI DZIKO
LAPANSI?

**WOPUSA
IWE!**

CHIFUKWA CHA
TCHIMO. MUYENERA KULEKA
KUCHIMWA NDIPO MUZIKONDA
ANZANU NDI KUWACHITIRA
CHILUNGAMO.

PATAPITA ZAKA 120, BWATO LIJA
LITAPANGIDWA, MULLUNGU
ADAMBWERETSERA NOWA NYAMA
ZOSIYANASIYANA KUCHOKERA KU
MBALI ZONSE ZA DZIKO LAPANSI.

ONANI, NYAMA
ZAMBIRI ZOSIYANASIYANA.
ZIKUBWERA ZOKHA, NGATI
KUTI WINA AKUZIITANA.

SIZINGATHEKE.
NKUTI KUMENE
MUNGAKATENGE
MADZI OTI
NKUCHITITSA
CHIGUMULA DZIKO
LONSE
LAPANSI?

ZINA ZILI NDI
MAONEKEDWE
ACHILENDO.
SINDINKADZIWA
KUTI KULINSO
NYAMA ZOTERE.
KODI NKUTHEKA
KUCHITIKADI ZIJA
NOWA AKUNENA
ZOTI MULLUNGU
ADZATUMIZA
CHIGUMULA?


GENESIS 7:7-9; 2 PETRO 2:5



MALO ATSALA
OCHEZA ZEDI.

IZO
NDI NYAMA
ZOMALIZA.

**NTHAWI NDIYE YAKWANA.
BWERA DZALOWE M'BWATOMU
PAMODZI NDI BANJA LAKO, NDI
NYAMA ZAKO. POSACHEDWAPA
ANTHU AMENE AKUKANA KULEKA
MACHIMOWA ANONG'ONEZA
BONDO.**




MULUNGU ANATSEKA
CHITSEKO CHA BWATOLO
NDIPO PA MASIKU 7
PALIBE CHIMENE
CHIDAACHITIKA.

HA, HA, TAONANI
ANTHU OPUKA!
ADZITSEKERA M'BWATO
LALIKULU NDI NYAMA ZIJA,
M'CHIGWA CHOLIMA,
KUTALI ZEDI NDI KUMENE
KUMAKHALA MADZI.

AKHALA
M'MENEMO
KWA SABATA
IMODZI
TSOPANO!

NKUTHEKA
KUTI MIKANGO
YAWADYA KALE.




MULUNGU ANATSEKA
CHITSEKO CHA BWATOLO
NDIPO PA MASIKU 7
PALIBE CHIMENE
CHIDAACHITIKA.

HA, HA, TAONANI
ANTHU OPUSA!
ADZITSEKERA M'BWATO
LALIKULU NDI NYAMA ZIJA,
M'CHIGWA CHOLUMA,
KUTALI ZEDI NDI KUMENE
KUMAKHALA MADZI.

AKHALA
M'MENEMO
KWA SABATA
IMODZI
TSOPANO!

NKUTHEKA
KUTI MIKANGO
YAWADYA KALE.



ZOTEREZI
SINDINAZIONEPO; KODI
KAPENA ANTHU AMISALA
AMENE ALI M'BWATOMO
ANKANENA ZOONA KUTI
MULLINGU AFUNA KUONONGA
ANTHU ONSE CHIFUKWA
CHA MACHIMO AO?

KOMA PA TSIKU LA 7 MVULA
INAYAMBA KUGWA NDIPO
NAWO MADZI A PANSI PA
DZIKO ANATUMPHUKA.

AKA KADAALI KOYAMBA KUTI MVULA IGWE
CHILENGEDWERE CHA DZIKO LAPANSI. NYENGO
INALI YABWINO NTHAWI ZONSE NDIPO CHINYONTHO
CHINKACHOKERA PANSI KUTHIRIRA NTHAKA. PALIBE
AMENE ADAAONAPO KAPENA KUMVA ZA MVULA,
NCHIFUKWA CHAKE ANTHU AMBIRI ANKATI NOWA
ANALI WAMISALA POGANIZA KUTI MADZI
ADZACHOKERA MU MLENGALENGA, KOMA NOWA
ADAKHULUPIRIRA ZIMENE MULUNGU ADAANENA.



SICHONCHO;
MULUNGU NDI AMAKONDA
ANTHU ONSE. MUNTHU
MMODZI ANGAKHALE
WOLUNGAMA BWANJI
KUPOSA ATSOGOLERI ATHU
A CHIPEMBEDZO?



NDIKADAMVERA
NOWA UJA. NDASANDUKA
WOPUSA ZEDI!

MULUNGU,
PULUMUTSANI
MWANA WANGA!

GENESIS 7:9-11, 16

A dramatic illustration of a massive flood. The scene is filled with turbulent, dark blue water. In the background, a bright light breaks through the rain, illuminating a small boat or structure. In the foreground, several people are struggling in the water, some appearing to be in distress. The overall atmosphere is one of chaos and peril.

PAFUPIFUPI 2348 B.C.

ANTHU ANAZINDIKIRA
NTHAWI ITATHA KALE KUTI
NOWA ANKANENA ZOONA.

MVULA INAGWA KWA MASIKU 40,
USANA NDI USIKU MPAKA MADZI
ANAPHIMBA PHIRI LILILONSE PA
DZIKO LONSE LAPANSI. ZOPUMA
ZONSE ZINAFU, KUPATULA
ZOKHAZO ZIMENE ZIDAALI NDI
NOWA M'BWATO MUJA.
ADAKHALA M'BWATO MUJA
MASIKU AMBIRIMBIRI.

MVULA INAGWA KWA MASIKU 40,
USANA NDI USIKU MPAKA MADZI
ANAPHIMBA PHIRI LILILONSE PA
DZIKO LONSE LAPANSI. ZOPUMA
ZONSE ZINAFU, KUPATULA
ZOKHAZO ZIMENE ZIDAALI NDI
NOWA M'BWATO MUJA.
ADAKHALA M'BWATO MUJA
MASIKU AMBIRIMBIRI.



NDIDZAKONDWERA
MADZI AKADZAPHWA,
IFE NKUTULUKA
M'BWATO MUNO.

POMALIZA NOWA ADATULUTSA NKHUNDA
M'BWATO MUJA NDIPO IDAABWERA NDI
NTHAMBI KUKAMWA, KWAKE KUSONYEZA KUTI
PENA PAKE PANALI MTENGO WOMWE
UNKAPHUKA. ADAITULUTSANSO PAMBUYO PAKE,
KOMA ULENDU UNO SINABWERERE, KUSONYEZA
KUTI IDAAPEZA MALO ABWINO OKHALA.



GENESIS 7:12, 19-23, 8:9-11



POSAKHALITSA BWATO LIJA
LINABWATAMA PAMWAMBA PA
PHIRI LOTCHEDWA ARARATI.
ALIYENSE ADATULUKIRA KU
DZIKO LATSOPANO-DZIKO
LOPANDA UCHIMO.



NOWA ANAMANGA GUWA LANSEMBE
NAPEREKERAPO NSEMBE ZA NYAMA. NGAKHALE
NOWA ANALI WOLUNGAMA, MUMTIMA MWAKE
MUNALI UCHIMO NDITHU. NSEMBE ZAMAGAZIZI
ZINKAPEREKEDWA KWA MULUNGU M'MALO MWA
MOYO WA NOWA NDI BANJA LAKE.

NYAMA ZISANU NDI ZITATU
ZIKUIMIRA ANTHU ASANU NDI ATATU
AMENE AKANAFI NDI CHIGUMULA
CHIJA KOMA ANAPULUMUKA
CHIFUKWA CHA CHISOMO CHA
MULUNGU. ZIKUFANANAKO NDI
ZIMENE MULUNGU ADACHITA
M'MUNDA WA EDENI MUJA PAMENE
ADAPHA NYAMA NDI KUPANGIRA
ZOVALA ZA ADAMU NDI HAVA.



**NDIDZAIKA UTAWALEZA
MUMLENGALENGA KUTI UKHALE
CHIZINDIKIRO CHAKUTI
SINDIDZAONONGANSO DZIKO
LAPANSI NDI MADZI. MUKHALE NDI
ANA AMBIRI NDIPO MUMWAZIKANE
NDI KUDZAZA DZIKO LAPANSI.**





**NDIDZACHITITSA
KUTI NYAMA ZIZIOPA
ANTHU. MUYENERA
KUDYA CHOLENGEDWA
CHILICHONSE CHAMOYO
NDI CHOKWAWA PA DZIKO
LAPANSI, MONGA MOMWE
MUMADYERA NDIWO
ZAMASAMBA NDI ZINA
ZOTERE. KOMA MUSADYE
MAGAZI A CHOLENDEDWA
CHILICHONSE. MUSAPHE
MUNTHU ALIYENSE.**



**NGATI WINA WAPEZEKA NDI
MLANDU WOPHA MNZAKE ANTHU ENA
AYENERA KUMUPHA. NGATI MUNTHU AKHETSA
MWAZI WA MNZAKE, ANTHU ENA AYENERA
KUKHETSA MWAZI WAKE KUTI ALIPIRE MLANDU
WAKE, CHIFUKWA MOYO ULI M'MWAZI.**



NOWA ANALI MLIMI NDIPO
ANABZALA MPESA. PA DZIKO
LAPANSI PANALI MABANJA ANAI
OKHA. KOMA KENAKA ANA A NOWA
ANAYAMBA KUBEREKA ANA AONSO.


GENESIS 8:4, 20, 9:1-29



NOWA ADAONA KUTI AKAIKA CHIPATSO M'KONTENA NDI KUCHISIYA OSACHIDYA KWA MASABATA ANGAPO, CHIMAPANGA CHAKUMWA CHOLEDZERETSA CHIMENE AMATI AKAMWA CHIMAMPATSA CHIMWEMWE. NOWA ADAYAMBA KUKONDA CHAKUMWACHO NDIPO NTHAWI ZINA SANKATHA KUGWIRA NTCHITO. ANKAGONA NGATI WAFWA. CHINKAMUCHITITSA ZINTHU ZOSAKONDWERETSA MULLINGU.

TSIKU LINA NOWA ADALEDZERA NDIPO
ADAVULA ZOVALA ZAKE NATULUKA PANJA.
HAMU ADAONA MALISECHE A ATATE AKE
NAYAMBA KUSEKA. ADAUZA ABALE AKE
MONYOGODOLA ZA ZIMENE ADAZIONAZO.





NOWA
ATADZUKA,
ANA AKE ENA
ANAMUUZA
ZIMENE HAMU
ADAACHITA.

PATAPITA ZAKA
ZAMBIRI ULOSI WAKE
UDAKWANIRITSIDWA.

MWANA WAKO
KANANI NDI ZIDZUKULU
ZAKE ADZAKHALA AKAPOLO
A ZIDZUKULU ZA MBALE
WAKO SEMU.

GENESIS 9:21-27; 1 MBIRI 4:40; SALIMO 78:51, 105:23, 27, 106:22

SETI

ADAMU NDI HAVA




KAINI



ABELE

NOWA NDI BANJA LAKE ADAPEZA CHISOMO PAMASO PA MULLINGU.



MULLINGU ANAPHA ANTHU ONSE KUPATULAKO ANTHU ASANU NDI ATATU AJA.

PA NTHAWIYO YAFETE ANAPITA KUMADZULO NDI KUMPOTO NAKABEREKAKO ANA. SEMU ANAPITA KUMMAWA NAKAKHALA KU ASIYA. HAMU ANAPITA KUMMWERE NAKAKHALA KU AFIRIKA NDI KUMMWERE KWA ASIYA. ZIDZUKULU ZA MWANA WAKE KANANI ZINAKAKHALA KUMENE LERO LINO TIMATI KU PALESITINA. NDIPO DZIKO LINADZALA NDI ANTHU.

PAFUPIFUPI 2247 B.C.

HAMU, MWANA WA NOWA, ANALI NDI MWANA DZINA LAKE KUSI, NDIPO KUSI ANALI NDI MWANA DZINA LAKE NIMURODI. NIMURODI ANAKULA NAKHALA MLENJE WAMPHAMVU NDIPO ANATCHUKA PA DZIKO LONSE LAPANSI. ANKAKANA KUMVERA MULUNGU NDIPO ANAYAMBITSA CHIPEMBEDZO CHAKE CHABODZA M'DZIKO LA BABILONI.

ANTHU A KU BABILONI SANAFUNE KUMWAZIKA NDI KUDZAZA DZIKO LAPANSI MONGA MOMWE MULUNGU ANALAMULIRA, NDIPO ANAGWIRIZANA ZOMANGA NSANJA YAIKULU NDI YAITALI KUTI IKHALE MALO OPEMBEDZERAPO.





KOMA SANKAPEMBEDZA
MLENGI WAO. SATANA
ADAWATSOGOLERA KUTI
APANGE MILINGU
YAOYAO YA MITENGO,
MIYALA NDI CHITSULO.

MULLUNGU ANAKWIYA
CHIFUKWA CHOTI IWO
SANKAFUNA KUMWAZIKIRA
PA DZIKO LONSE LAPANSI.
CHONCHO ANAWACHITITSA
KUTI AZIYANKHULA
ZIYANKHULO ZAMBIRI
ZOSIYANASIYANA.




ᑲᑲᑲ ᑲᑲᑲ ᑲᑲᑲᑲ
ᑲᑲᑲᑲᑲᑲᑲᑲᑲ ᑲᑲᑲᑲ
ᑲᑲᑲ ᑲᑲᑲᑲᑲᑲᑲ

ᑲᑲᑲᑲ ᑲᑲᑲᑲ ᑲᑲᑲᑲ
ᑲᑲᑲᑲᑲᑲᑲᑲᑲᑲ ᑲᑲᑲᑲᑲᑲᑲ
ᑲᑲᑲᑲᑲᑲᑲᑲ

AMISIRI
SANKAMVETSETSANA
KOTERO KUTI KUNALI
KOVUTA KUTI APITIRIRE
NDI NTCHITO YAOYO.



ANTHU OFANANA ZIYANKHULO
ANAPITA KU DERA LAOLAO. ANTHU
ENA ANAPITA KUTALI, ENA
ANAYENDA PA SITIMA ZAPAMADZI
NAKAKHALA KU ZILUMBA ZAKUTALI,
ENA ANAPITA KUMPOTO KOZIZIRA,
NDIPO ENAANAPITA KU ZIPULULU
KOMWE KUNALI KOTENTHA.
CHONCHO LAMULO LA MULUNGU
LOTI ANTHU ADZAZE DZIKO LAPANSI
LINAKWANIRITSIDWA.



PAMENE DZIKO LAPANSI
LINADZALA NDI ANTHU,
UCHIMO UNAYAMBANSO
KUCHULLUKA. ANTHU
ANAYAMBA KUPEMBEDZA
MAFANO NDIPO ADAIWALA
MULUNGU WAMOYO.

GENESIS 10:6-10, 11:1-9



<https://goodandevilbook.com/>